Finnish TWR Women of Hope team at a Run for Missions event

Kupemphelel Kuyamika ndikulemekeza Mulungu Atate wathu

Chichewa

Ntchito za Yehova nzazikulu, zofunika ndi onse akukondwera nazo. Chochita Iye ncha ulemu, ndi ukulu: Ndi chilungamo chake chikhalitsa kosatha. Anachita chokumbukitsa zodabwitsa zake; Yehova ndiye wachisomo ndi nsoni zokoma*!* Masalimo 111:2–4.

Ndizofunika kulingalila za miyoyo yathu ndikukhala ndi nthawi yokumbukila kenako kuyamika ndikuthokoza Mulungu Atate wathu kaamba ka zonse watichitila. Wolemba Masalimo mundime zili m'mwambamu akukamba zoti Mulungu amatikumbutsa ntchito zake zodabwitsa. Kodi wolemba masalimo akuti chani pazokumbukila? Yehova ndiye wachisomo ndi nsoni zokoma*!*

Kodi inu mumayamika Mulungu chifukwa chani? Ndi zinthu ziti zomwe mukakumbukila zimabweletsa Chimwemwe ndi mayamiko mumtima mwanu mukakumbukila mene Mulungu anakupatsilani zosowa zanu? Machilitso, chitonthozo, Chikondi, ufulu omwe Mulungu wakupatsani?

Mayamiko athu sakutengela madalitso omwe Mulungu. Mmoyo nthawi zambiri umakhala ovuta komanso timakumana ndi zopinga. Kodi ndi malo ovuta otani omwe timakhalamo ingakhale titapemphela, kuzindikila kuti Mulungu amakhalabe nawe ndipo Iye ndi Chiyembekezo ndi mtendere ingakhale tikuvutika?

Mwezi uno tikulemekeza Mulungu kaamba ka zomwe akuchita ku TWR mayi wa chiyembekezo. Magulu ambiri akulemba ndikukonza okha mapulogalamu. Magulu opembedera akutumikila anthu omwe ayandikana nawo, anthu aku ndende komanso omwe amazembetsedwa. Mbeu ya mau a Mulungu ikudzalidwa ndipo kukula m'mitima ya omvera!

Nde tikuthandizana ndi wolemba Masalimo pofuula ndi Chimwemwe kwa Mulungu. Tikuyamika ndi Kulemekeza Iye pokhala mlengi wathu wabwino yemwe watitenga ife ngati anthu ake ndikutikonda ndi Chikondi chosatha.

Fuulirani kwa Yehova, inu, dziko lonse lapansi. Tumikirani Yehova ndi chikondwerero:
Idzani pamaso pake ndi kumuimbira mokondwera. Dziwani kuti Yehova ndiye Mulungu; Iyeyu anatilenga, ndipo ife ndife ake; ndife anthu ake ndi nkhosa zapabusa pake. Lowani kuzipata zake ndi chiyamiko, ndi kumabwalo ake ndi chilemekezo:
Myamikeni; lilemekezeni dzina lake. Pakuti Yehova ndiye wabwino; chifundo chake chimanka muyaya; ndi chikhulupiriko chake ku mibadwomibadwo. (Masalimo 100)

Atate, Tikulemekezani ndikukuyamikani ... November 2019

1. … Wophunzila wachigawo chapakati ku Asia yemwe anafikila gulu la mayi wa Chiyembekezo ku Norway. Anawalimbikitsa kuti apitilize kukhala okhulupilikilika pamene mapulogalamu awo ndi amene anamuthandiza nthawi imene iye anali mkhritsu yekhayo mmudzi mwawo.	**2.** … kukula kwa chiwelengelo cha anthu omwe amamvela pulogalamu ya mayi wa chiyembekezo pa tsamba la Facebook ku Romania. Gulu la mayi wa chiyemebekezo likufikila anthu azaka, maphunzilo komanso zipembedzo zosiyana siyana kudzela pa tsamba la Facebook.	**3.** … tikukusankha kubukitsa dzina lanu. yamikani Yehova, itanirani pa dzina lake; bukitsani mwa mitundu ya anthu zochita Iye. Muimbireni, muimbireni zomlemekeza; fotokozerani zodabwitsa zake zonse. (Masalimo. 105:1-2).
4. … kuti mayi wa Chiyembekezo ku Tanzania ikuwulutsidwa mu Chiswahili kumawayilesi Khumi. Atate, akudziweni ngati mbuye ndi mpulumutsi wawo komanso akhale pa ubwenzi ozama ndi inu kudzela mukuulutsidwa kwa mapulogalamuwa.	**5.** … kuti gulu la TWR mayi wa chiyembekezo likachita likutenga nawo mbali pazochitika ku ndende zaku Romania pamene kukhale nthawi yamasewero mu November. Tikupemphe kuti chilungamo chanu chikapelekedwa mwachindunji kwa akaidi ndikuti akathe kukukomelani.	**6.** … kuti pulogalamu ya mayi wa chiyembekezo ku Indonesia iwulutsidwe mumawayilesi 46 ndi mapulogalamu a Javanese kumawayilesi 22. Pafupifupi madela onse ku Indonesia akufikilidwa ndipo zikupeleka mwayi kwa anthu osakhulupilila kuti amve mau a Mulungu.
7. … kuti ulendo wothamanga wa ntchito za Mission ku Finland unapeza ndalama za TWR mayi wa Chiyembekezo ku India. Gulu laku Finland ndilothokoza kaamba ka ufulu olankhula za Yesu komanso ntchito zawo zofikila ena ndi uthenga wabwino.	**8.** … kupeleka malo okhala kwa amayi omwe anazembetsedwa ku Albania. Komanso gulu la TWR mayi wa chiyembekezo linakwanitsa kugawa uthenga wabwino komanso ma pulogalamu a chuma chobisika ndi amayi asanu ndi anayi omwe anazembetsedwa.	**9.** … kuti uthenga wabwino ukufalitsidwa ku Ukraine. Tikuyamika alongo anthu omwe amapita ku chipatala, masukulu ogonela konko ndikuphunzitsa makhalidwe achikhritsu kumasukulu. Mau anu apite ndi Mphamvu!
10. … Mwa ichinso Mulungu anamkwezetsa Iye, nampatsa dzina limene liposa maina onse, kuti m'dzina la Yesu bondo lililonse lipinde, la za m'mwamba ndi za padziko, ndi za pansi padziko, ndi malilime onse avomere kuti Yesu Khristu ali Ambuye, kuchitira ulemu Mulungu Atate. (Afilipe. 2:9-11).	**11.** … amayi ambiri omwe analowa gulu lopembedzela ku Serbia chiyambileni gululi mwezi wa March chaka chino. Mulungu akulimbikitsa mitima yawo pamene akupemphelela amayi omwe akudutsa munyengo zowawa padziko lonse.	**12.** … kuti anthu ogwila ntchito mozipeleka ku Africa omwe akulimikizana ndi magulu a TWR mayi wa Chiyembekezo. Mumikumano yawo amayi akulumikizana ndikugawana zomwe zili mmitima mwawo.
13. …njira imene magulu opembedzela a TWR mayi wa Chiyembekezo akutumikila ndikuphunzitsa anthu omwe ali kundende. Atate, chitani ntchito yopambana yoyeletsa ndikubwenzeletsa moyo weniweni kwa amayi ndi abambowa.	**14.** … abambo ndi amayi omwe akukuza opembedzela amamphamvu ku France. Mubweletse opembedzela ambiri kuti agwile nawo ntchito , Atate ndikuwathandiza kukhala okhulupilika pofuna nkhope Yanu.	**15.** … mukugwila ntchito mmidzi yaku Malawi ndikutsegula makomo a Utumiki. Tikukuyamikani kaamba ka Abusa omwe akumakumana ndikupemphela ndi amayi 200 ndipo akutumikila amayi amasiye.
16. … kuti ndinu mwini Moyo. Ndife oyamika kuti patadutsa zaka zisanu zokanizidwa, phwando la life and March linachitika pa 14 September 2019 ku Zurich Switzerland.	**17.** … Chifukwa chake monga momwe munalandira Khristu Yesu Ambuye, muyende mwa Iye, ozika mizu ndi omangiririka mwa Iye, ndi okhazikika m'chikhulupiriro, monga munaphunzitsidwa, ndi kuchulukitsa chiyamiko. (Akolose. 2:6-7).	**18.** … kuti pulogalamu ya mayi wa Chiyembekezo ikuwulutsidwa muchilankhulo cha Tamil. Mauthengawa amaphunzitsa ndikupeleka upangili kwa amayi komanso kudalitsa abambo omwe amvela.
19. … kuti malonjezano amu a Mulungu ndioona ndiodalilika. Ambuye mumaona mazunzo omwe munthu wina aliyense amadutsamo. Ndipo akafuulila kwa Inu mumamva ndikulowelela mu nyengo zawo.	**20.** … pulogalamu ya chuma chobisika yomwe ikukonzedwa muchilankhulo chaku Korea. Tipemphele kuti igwilitsidwa ntchito kutumikila amayi kumpoto kwa Korean omwe akukhala ku China.	**21.** … anthu opembedzela ku Canada omwe amapembedzela mapemphelo omwe amayi amatumiza mapempho amapemphelo tsiku lili lonse. Tikuyamikanso anthu omwe amagwila ntchito mongozipeleka ndi mokhulupilika pokonza mauthenga otumiza mwezi uliwonse.
22. … mapulogalamu a Hanna's Café akukonzedwa ndipo amayi omwe ali pakakasi akusinthika kukhala amayi omwe amatha kudzikhulupilila okha komanso kukhala ndi chiyembekezo.	**23.** … omvela pulogamu ya mayi wa chiyembekezo ku Portugal. Amalumikizana ndi gulu la mayi wa chiyembekezo kuwafotokozela mene pulogalamuyi ikudalitsila miyoyo yawo.	**24.** … ndife osankhidwa ndi oyela komanso opanda chilema pamaso pa Mulungu. Tinawomboledwa ndikukhululukidwa mwa chisomo cha Khritsu. Tinasindikizidwa chizindikiro ndi Mzimu Woyera wa lonjezano. (Aefeso. 1:4-13)
25. … pulogalamu ya mayi wa Chiyembekezo ku Ethiopia ikhala ikukondwelela zaka khumi mu utumiki mwezi wa January 2019. Atate pitilizani kutsogolela ndikupeleka zofuna za utumikiwu.	**26.** … kuti tikondwele nthawi zonse, kupemphela mosaleka ndikuthokoza munyengo zonse poti ichi ndi chifunilo chanu pa ife mwa Khritsu Yesu. (1 Atesolonika. 5:16-18).	**27.** … potumiza gulu kum'mawa chakumpoto kwa Asia lomwe limakonza mwaluso pulogalamu ya mayi wa chiyembekezo muchi Vietnamese ndi chi Japanese.
28. … magulu ang'ono ang'ono ndi mabungwe omwe ali okonzeka kugawa mapulogalamu a chuma chobisika kumadela aku Germany.	**29.** … zaka 60 zamgwilizano pakati pa TWR ndi ERF ku Germany,komanso thandizo la ERF's ku TWR mayi wa Chiyembekezo chiyambileni pulogalamuyi.	**30.** … Chifukwa chake musadere nkhawa, ndi kuti, Tidzadya chiyani? Kapena, Tidzamwa chiyani? Kapena, Tidzavala chiyani? 32Pakuti anthu akunja azifunitsa zonse zimenezo; pakuti Atate wanu wa Kumwamba adziwa kuti musowa zonse zimenezo. (Mateyu. 6:31-32)